- **MPHEKESELA ZABODZA PAZOKHUDZANA NDI MILEME**
  Mileme Imafalitsa matenda Ambili- Izi ndizabodza, mileme ndi nyama zawukhondo ndipo sizifalitsa matenda, pokha pokha atadya mleme kapena atalumidwa ndi mleme'wu
- ***Mileme imafalitsa Ebola*** – Ndi mileme yochepa kwambili imene imanyamula ebola, Mileme ina yobwela kuchokela kumaiko ena ikhoza kunyamula ebola, koma munthu akhoza kutenga pokha pokha atadya mleme'wo. Ndipo kumalaiw kulibe umboni oti mileme ili ndi ebola.
- ***Mileme yonse ili ndi chiwewe*** - Ndi mileme yochepa kwambiri ingakhale ndi chiwewe koma munthu sangatenge ngati sanayigwire. Kupewa mileme kumathandiza kupewanso matendawa.
- **Mileme si ya khungu**-Mileme imawulika usiku ndipo imaona bwino kwambiri. Mileme yambiri imaona bwino kuposa anthu usiku
- **Mileme si mbewa zouluka** – Palibe ubale ngakhale pan'gono pakati pa mbewa ndi mileme – mileme ndinyama zoyamwitsa koma zachilengedwe chakechake.
- **Simileme Yonse Imayamwa Magazi**- mwa mitundu yamileme yoposela 1300, itatu yokha ndiyo imayamwa magazi, ndipo simapezeka kumalawi, iyo imapezeka kumaiko a aluya

Mileme ndi nyama zofunikila pachilengedwe chadziko lapansi, ndipo ikuenela kutetezedwa, tikapanda kuiteteza, tizakhala pachiophyezo chosowelatu zipaso ndi zomela zina nzina, ngati titeteza mileme tizasangalala ndi phindu mu ulimi wathu, ndi kuchepesa tizilombo tomwe timatisowetsa ntendele

MUKUFUNA CHITHANDIZO PA ZAMILEME?

Tiimbileni pa lamya yathu mwaulele pa **5152** kuti mulandile chithandizo choenekela

THILILANI ZAKUMUNDA KWANU NDIMANYOWA A MILEME MWAULELE

Ndowe zamilime ndimanyowa aulele amene amaonjezela kuchulutsa zokolola zanu, komanso kubwezeletsa chonde munthaka

UBWINO WAMANYOWA A MILEME:

- Kubwezeletsa Chonde Munthaka
- Amalemetsa kapena kuti Kutsuka Nthaka
- Amachepetsa madzi osefukila minda mwathu
- Ndimankhwala achilengedwe othandiza kupha tizilombo toononga mizu ndi mbewu zathu kumunda
- Amapangisa kuti manyowa athu awolelane mwachangu munthaka

MANYOWA MILEME NGATI CHAKUDYA CHA MBEWU

- Manyowa amilime ali ndi mlingo wa 10% nitrogen, 3% phosphorus, ndi 1% potassium (Bat Guano NPK=10:3:1).
- **Nitrogen amapangitsa kuti zomela zathu zikule mwachangu komanso zizioneka mobiliwila bwino**.
- **Phosphorus amapangitsa kuti mizu ya mbewu zathu izikula mwathanzi komanso kuthandiza kakulidwe kakuliidwe amalauwa, ndipo potassium amathandiza kuti tsinde kapena kuti Matunthu ambeu azikula ndimphavu.**

KAGWILITSIDWE KA NDOWE ZAMILEME NGATI MANYOWA

Ngati Manyowa Obeleketsa: Pali njila ziwili zimene tingagwilitse ndowe zamileme ngati manyowa obeleketsa:

1. Phimbilani munda wanu ndiudzu, mapesi, ndizina zotelo, ndipo mwanzani manyowa anu pamwamba pawudzupo nkuthilapo madzi kuti pakhale Chinyontho. Izi zimapangitsa kuti tizilombo tooletsa manyowa athu tigwile ntchito mwachangu kupangisanso kuti manyowa anthu asachedwe kuphya munthaka, nkuonjezela chakudya munthaka mwachangu
2. Njila ina; thilani manyowa anu mozungulila mbeu yanu, ndipo mukatelo thilani madzi mozungulila mbeu'yo.

Manyowa amilime amadzi

- Phatikizani kapu imodzi ya manyowa anu, ndi muyeso wamadzi okwanila pafupi fupi malitala asanu, mukatelo manyowa anu amadzi ngokonzeka kuthilila zomela zanu

NTHAW YAKATHILIDWE

- Onetsetsani kuti manyowa anu athilidwe ma m'bandakucha

PHINDU LA MILEME MU ULIMI WATHU

- Mileme imadya tizilombo timene timaononga zakumunda kwathu, Pakutelo mileme imathandiza kuonjezela zokolola zathu, komanso imathandiza kuchepesa kudalila mankhwala othila kuminda kwathu oti aphe tizilombo, mwachoncho kumuthandiza mulimi kuti asaononge ndalama zogulila mankhwala.
- Kusagwilitsa ntchito kwambili mankhwala amakono kuminda kwathu kumathandizanso kuti tisaononge mpweya omwe timapuma komanso madzi omwe timagwilisa ntchito.

KUNVETSETSA ZOKHUDZANA NDI MILEME

- Milime zimayamwitsa ana ake ngati ife anthu, ngakhale izi zilichonchi, timasiyana chifukwa mileme ili ndiluntha lowuluka.
- Mileme ili ndi bweya ngati nyama ina iliyonse yomwe imayamwitsa
- Mileme imadyedwa ndi njoka, akadzidzi, kantema komanso ziombankhanga

Zeni zeni zokhudza Mileme

- Pali mitundu yoponsa 1300 ya milime padziko lapansi lonse
- Kumalawi kuno tili ndi mitundu ya mileme yokwana 64!
- Bats on average give birth to 1 or 2 offspring a year
- Mleme umabeleka ana osaposela awili pa chaka
- Mleme umodzi waukulu umadya tizilombo kuphatikizilapo udzudzu tokwana 500 usiku umodzi

African Bat Conservation works conducts applied research and community outreach to conserve bats in Malawi.

Pitani ku www.africanbatconservation.org kuti mudziwe zambili zonkhudzana ndi mileme yaku malawi Kapena tiimbileni pa lamya iyi **5152** mwaulele.